

# **Katekisimu wa Chiphunzitso**

## **Katekisimu wa Ana**

### **Kudziwitsidwa za Katekisimu wa Chidule wa Westminister**

Amene analemba koyambirira sakudziwikabe mpaka pano  
Lakonzedwa ndi kukulitsidwa malemba ake ndi **Pastor J.J.Lim**  
Mwaonjezeredwanso mfundo zina ndi **Pastor David Higgs**

Latanthauziridwa mu Chichewa ndi **W. Chapasuka** komanso **A. Mkwinda**  
Lakonzedwa mu Chichewa ndi **Rev. Rex Chitekwe** komanso **Rev. Precious Kanyowa**

December 2010 edition

## **Katekisimu wa ana ang'ono- Kudziwitsidwa za Chidule cha Katekisimu wa Westminster**

Amene analemba koyambirira sakudziwikabe mpaka pano  
Lakonzedwa ndi kukulitsidwa malemba ake ndi **Pastor J.J.Lim**  
Mwaonjezeredwanso mfundo zina ndi **Pastor David Higgs**

Latanthauziridwa mu Chichewa ndi **W. Chapasuka** ndi **A. Mkwinda**  
Lakonzedwa mu Chichewa ndi **Rev. Rex Chitekwe** ndi **Rev. Precious Kanyowa**

Bukuli lasindikizidwa mu 2010 ndipo eni ake ndi a Pilgrim Covenant Church.

Chichewa version © 2012 Gratia Dei Sola Media  
Lasindikizidwa ndi Grata Dei Sola Media  
Blk 203B, Henderson Road , #07-07, Singapore 159546  
Website: [www.gdsmedia.org](http://www.gdsmedia.org)  
Email: [gdsmedia.sg@gmail.com](mailto:gdsmedia.sg@gmail.com)

Palibe akuloledwa kusindikiza kapena kuchulukitsa buku ili ngakhale za mkatimu

**Synod ya Evangelical Presbyterian Church (EPC) ku Malawi ndi ku Mozambique  
inavomereza mu chaka cha 2012 kuti bukuli lizigwiritsidwa  
ntchito mu mipingo yawo yonse.**

## **Mau oyambilira**

Maziko a chipunxitso a katekisimu akuchokera pamene mtumwi Paulo adalamula Timoteo kuti "gwiritsitsa ( ndi chikhulupiliro ndi chikondi cha Yesu Khristu) mawu amphanvu" amene adawamva kuchokera kwa iyeyo. (2 Tim 1: 13)

Kuti tipunxitse bwino katekisimuyu kwa ana athu, tigwiritse ntchito mabuku a *Katekisimu wa Mbiri ya Baibulo* ndi *Katekisimu wa chipunxitso a Baibulo*.

*Katekisimu wa Mbiri ya Baibulo* akulondola mbiri ya chipulumutso m'Buku Lopatulika pamene *Katikisimu wa Maphunxitso a Baibulo* amangofotokoza mwachidule maphunxitso ofunika a m'Buku Lopatulika kukhala zimene ziunika kuti zizichitika.

Tidasankha makatekisimu awiri a maphunxitso kuti tizigwiritsa ntchito mtchalichi pofuna kuphunzitsira ana athu. Awa ndi *Katekisimu Wachidule wa Westminister* ndi *Katekisimu wa Ana Aang'ono*. *Katekisimu wa ana ang'onoyu* wakonzedwa kuti awalunzanitse ndi kuwapatsa chiyambi cha *Katekisimu Wachiduleyu*.

Pamene cholinga chathu nkufuna kuti ana athu akumbukire kwa nthawi yaitali *Katekisimu Wachidule*, tikuona kuti ndi bwino kuti ana amene sangathe kumvetsa bwino Katekisimuyu aphunzire zowathandiza kumvetsa Katekisimuyu zogwirizana ndi msinkhu wawo. Makolo amene akuona kuti ana awo angathe kuloweza pamtima Katekisimu Wachiduleyu (asanafike pomvetsa bwinobwino) angathe kuwaphunzitsa kuloweza pamtima *Katekisimu Wachiduleyu* pamene akugwiritsa ntchito kabuku kano.

Ndifuna ndinene motsindika pano kuti udindo ophunzitsa ana ndi wa makolo (makamaka abambo). Aphunzitsi athu akatekisimu adzangophunzitsa mwachidule ndi kuwafunsa mafunso pazomwe alloweza msabata imeneyo. Abambo akupemphedwa kufotokozena ana awo mayankho onse anawo asanaphunzire ndi aphunzitsi awo.

Mulungu Atate athu a Kumwamba adalitse ana athuwa kuti choona cha Mawu Ake chisungike mmitima mwawo mpaka mibadwo yamtsogolo kuti Dzina Lake lilemekezedwe.

**- Pastor J.J. Lim**

**PHUNZIRO 1**  
**MULUNGU WA MOYO NDI WOONA-1**

**1. Adakulengani ndani?**

Mulungu.

**2. Chifukwa chiyani Mulungu adakulengani?**

Kuti mumbwezere ulemu wake, ndi kuti mukondwere naye kwa nthawi zonse.

**3. Mungambwezere Mulungu bwanji ulemu wake?**

PoMukonda ndi kutsatira malamulo ake.

**4. Chifukwa chiyani muyenera kumulemekeza Mulungu?**

Popeza adakulengani ndipo amakusamalirani.

**5. Kodi iripo milungu ina kupambana mmodzi yekha?**

Alipo Mulungu mmodzi yekha, wamoyo ndi woona.

**6. Nanga mafano a zosema ndi za miyala?**

Ndi milungu yonama imeneyo.

**7. Mwa Mulungu wa Moyo ndi Woona muli Anthu angati?**

Atatu.

**8. Anthu atatuwo ndiwo ati?**

Atate, Mwana ndi Mzimu Woyeria.

**9. Mumaphunzira kuti kukonda ndi kumvera Mulungu?**

M'baibulo lokha basi.

**10. Ndani adalemba Baibulo?**

Anthu woyeria omwe anauziridwa ndi Mzimu Woyeria.

*Vesi loloweza pamtima:*

“Koma Chauta ndiye Mulungu woona, Iyeyo  
ndiye Mulungu wa moyo, ndiponso Mfumu yamuyaya.” (Yer 10:10)

**PHUNZIRO 2**  
**MULUNGU WAMOYO NDI WOONA-2**

**11. Mulungu ndi ndani?**

Mulungu ndi mzimu wokhawokha, wachikhalire wopanda malire, wamuyaya ndi wosasinthika.

**12. Chifukwa chiyani Mulungu ali Mzimu wokhawokha?**

Chifukwa alibe thupi ngati la anthu.

**13. Chifukwa chiyani Mulungu ali wopanda malire?**

amapezeka paliponse, nthawi zonse.

**14. Chifukwa chiyani Mulungu ali wachikhalire?**

Alibe chiyambi ndi malekezero.

**15. Chifukwa chiyani ali wosasinthika?**

Chifukwa ndi wabwino nthawi zonse, sangakome kapena kuyipa kuposa mmene aliri kapena kusintha maganizo ake.

**16. Mulungu amapezeka kuti?**

Pena paliponse.

**17. Kodi Mulungu tingamuone?**

Ayi, Mulungu sindingathe kumuona, koma iye amandiwona nthawi zonse.

**18. Kodi Mulungu amadziwa zonse?**

Inde, palibe chobisika pamaso pa Mulungu.

**19. Kodi Mulungu angathe kuchita china chirichonse?**

Inde, Mulungu angathe kuchita china chirichonse malingana ndi chifuniro chake.

*Vesi loloweza pa mtima:*

“Mulungu ndi Mzimu, ndipo omulambira lye ayenera kumulambira mumzimu ndi mchoonadi.” (Yoh 4:24)

**PHUNZIRO 3**  
**CHILENGEDWE NDI MMENE MULUNGU ASAMALILIRA ZOLENGEDWA**

**20. Kodi mphamvu zake za Mulungu ndi zotani?**

Ndi dongosolo la Mulungu la dziko la kumwamba ndi la pansi pano asanalenge china chirichonse.

**21. Mulungu anakhala wachikhaliire kuyambira liti?**

Chinalipo kale Mulungu asanalenge zakumwamba ndi za pansi pano.

**22. Mulungu adaonetsa bwanji mphamvu yake?**

Pantchito yake yolenga dzikoli ndi kusamalira zolengedwa zonse.

**23. Ntchito ya zolengedwa zonse ndi yotani?**

Ndi ntchito ya Mulungu yolenga zonse osagwiritsa ntchito china chirichonse.

**24. Chilengedwe chinali chotani pachiyambi?**

Chinali chabwino zedi.

**25. Mulungu adalengeranji zinthu zonse?**

Chifukwa cha ulemelero wake,

**26. Ntchito ya kusamalira zolengedwa ndi yotani?**

Ndiko kukwaniritsa zonse zochitika m'dziko la kumwamba ndi la pansi pano.

**27. Chifukwa chiyani Mulungu amakwaniritsa zonse monga achitira?**

Chifukwa cha ulemelero wake komanso ubwino wa osankhidwa ake.

**28. Osankhidwa ake a Mulungu ndiwo ati?**

Amene Mulungu adawakonda kuchokera pa chiyambi.

*Vesi loloweza pa mtima:*

Mulungu ndine ndekha, palibenso wina ai; Ndithudi, Mulungu ndine, ndipo palibenso wina wonga Ine...Maganizo anga sadzalephera, ndipo ndidzachitadi zonse zimene ndidafuna kuchita.(Yesaya 46:9-10)

**PHUNZIRO 4**  
**MUNTHU NDI CHIPANGANO CHA NTCHITO**

**29. Mulungu adalenga bwanji munthu?**

Adapanga makolo athu oyambilira aja m'chifanizo chake.

**30. Makolo athu oyambilira anali ndani?**

Adamu ndi Eva

**31. Mulungu adapanga bwanji makolo athu oyambilira?**

Adapanga Adamu kuchokera ku dothi, ndipo Eva kuchokera ku thupi la Adamu.

**32. Atawapatsa thupi, Mulungu adawapatsanso chiyani Adamu ndi Eva?**

Adawapatsa mzimu wosafa konse.

**33. Kodi muli ndi mzimu komanso thupi?**

Inde, ndiri ndi mzimu komanso umene sudzafa konse.

**34. Mudziwa bwanji kuti muli ndi mzimu?**

Chifukwa Baibulo limandiuba choncho.

**35. Kodi Mulungu adampanga Adamu ndi Eva kukhala otani?**

Oyera ndi wosangalala.

**36. Chipangano ndi chiyani?**

Mgwirizano wa chikondi womangidwa ndi malonjezo pakati pa anthu awiri kapena kuposera apo.

**37. Kodi Mulungu adapanga chipangano chotani ndi Abrahamu?**

Chipangano cha Ntchito.

**38. Mulungu adafuna kuti Adamu achite chiyani m'Chipangano cha Ntchito?**

Kumvera Mulungu kotheratu.

**39. Mulungu adalonjeza zotani m' Chipangano cha Ntchito?**

Mulungu adamulonjeza Adamu moyo ngati amumvera lye.

**40. Mulungu adawopseza zotani m'pangano lake?**

Adzamulanga Adamu pombweretsera imfa ngati samumvera.

*Vesi loloweza pamtima:*

“Motero Mulungu adalenga munthu m'chifanizo chake, adawalengadi m'chifanizo cha Mulungu. Adawalenga wina wamwamuna wina wa mkazi.” (Gen 1:27)

**PHUNZIRO 5**  
**KUCHIMWA KWA ADAMU**

**41. Kodi Adamu adasunga Chipangano cha Ntchito?**

Ayi, adachimwira Mulungu.

**42. Tchimo ndi chiyani?**

Tchimo ndiko kukana kuchita chifuniro cha Mulungu kapena kuchita zomwe Mulungu aletsa.

**43. Kodi mawu oti 'kukana kumvera' atanthauzanji?**

Kusafuna kukhala kapena kuchita chomwe Mulungu afuna.

**44. Kukana kumvera ndiko kutani?**

Kuchita zomwe Mulungu aletsa.

**45. Tchimo la makolo athu oyamba aja ndi lotani?**

Adadya chipatso choletsedwa.

**46. Ndani adawanyenga kuti achimwe?**

M'dierekezi adamunyenga Eva ndipo chipatso china adakampatsa Adamu.

**47. Chidawachitikira n'chiyani Adamu ndi Eva atachimwa?**

Adasanduka ochimwa ndi osakondwa mmalo mokhala oyera ndi osangalala.

**48. Kodi Adamu adadziimirira yekha m'Chipangano cha Ntchito?**

Adaimilira mtundu wonse wa anthu ngakhale a pambuyo pake.

**49. Mtundu wa Adamu ndiwo ndani?**

Amuna onse, akazi onse ndi ana onse kuchokera pa Abrahamu kupatula Ambuye Yesu.

**50. Tchimo la Adamu lidabweretsa zotani kwa mtundu onse wa anthu?**

Anthu onse amabadwa ali ochimwa ndi omvetsa chisoni.

*Vesi loloweza pa mtima:*

“Ndidzaika chidani pakati pa iwe ndi mkazi, padzakhala chidani pakati pa mbeu yako ndi mbeu yake; idaphwanya mutu wako , ndipo udzaluma chitende chake. (Gen 3:15)

**PHUNZIRO 6**  
**TCHIMO LOYAMBILIRA**

**51. Tchimo limene ife timalitenga kwa Adamu limatchulidwa kuti chiyani?**

Tchimo loyambirira

**52. Tchimo loyambirira likupangidwa ndi chiyani?**

Kulakwa kwa tchimo la Adamu ndi kuyipa kwake.

**53. Kulakwa mwa Adamu ndiko kutani?**

Ndiko kukhala wochimwa pamaso pa Mulungu chifukwa cha Adamu.

**54. Kukhala mu uchimo ndiko kutani?**

Ndiko kukhala wochimwa mumtima mwanga ndi kuchimwa pa chirichonse chimene ndichita.

**55. Tchimo lirilonse limabweretsa chiyani?**

Mkwiyo ndi themberero la Mulungu.

**56. Tingathe kupulumuka tiri mu uchimo?**

Ayi, tiyenera kutembenuka mtima kuti tikhale oyenera kupita kumwamba.

**57. Kutembenuka mtima kumatchedwa chiyani?**

Kubadwano kachiwiri.

**58. Ndani angasinthe mtima wa munthu wochimwa?**

Mzimu Woyeraya yekha.

**59. Alipo angapulumutsidwe kudzera m'Chipangano cha Ntchito?**

Palibe angapulumutsidwe kudzera m'Chipangano cha Ntchito.

**60. Chifukwa chiyani palibe amene angapulumutsidwe kudzera m'Chipangano cha Ntchito?**

Chifukwa tonsefe tidaphwanya panganolo, choncho ndife oyenera kulangidwa.

*Vesi loloweza pamtima:*

Kale inu munali akufa chifukwa cha zolakwa zanu ndi machimo anu... n'chifukwachake mwa chibadwa chathu, tinali oyenera mkwiyo wa Mulungu monga ngati anthu ena onse. (Aef 2:1, 3b)

**PHUNZIRO 7**  
**PANGANO LA CHISOMO I**

**61. Kodi Mulungu Atate adapanga ndi yani Pangano la chisomo?**

Ndi Khristu, mwana wake wachikhaliire.

**62. Khristu adaimirira yani m'pangano la Chisomo?**

Anthu ake osankhidwa.

**63. Khristu adachita chiyani m'pangano la Chisomo?**

Kusunga malamulo mmalo mwa anthu ake, ndi kumva zowawa chifukwa cha machimo awo.

**64. Kodi Ambuye athu Yesu Khristu adadziwapo kanthu za kuyesedwa?**

Inde; lye adyesedwa mnjira zosiyanasiyana monga momwe tichitira ife.

**65. Kodi Ambuye Yesu adachita tchimo ngakhale lalin'gono?**

Ayi; lye adakhala woyeria, wopanda cholakwa china chilichonse komanso wosadetsedwa.

**66. Kodi Mwana wa Mulunguyu anayenera kumva zowawa?**

Khristu, Mwana wa Mulungu, anasanduka munthu kuti amvere ndi kumva zowawa za chilengedwe chathu.

**67. Kudzipereka nsembe ndiko kutani?**

Khristu adakwaniritsa chilungamo chake choyeria ndi masautso ake ndi imfa yake mmalo mwa ife ochimwa.

*Vesi loloweza pamtima:*

Koma nthawi itakwana, Mulungu adatuma Mwana wake, Mwanayo adabadwa mwa mkazi, adabadwa woyenera kumvera a Mose, Adachita zimenezi kuti akawombole amene anali akapolo a malamulowo ndipo kuti potero tisanduke ana a Mulungu. (Aga 4:4-5)

**PHUNZIRO 8**  
**PANGANO LACHISOMO II**

**68. Kodi Mulungu Atate adachita chiyani m'pangano la Chisomo?**

Kulungamitsa, kusandutsa ana ake ndi kuyeretsa onse amene Khristu anali kudzawafera.

**69. “Kulungamitsa” ndiko kutani?**

Ndiye cuti Mulungu wakhululukira ochimwa onse ndi kuwatenga ngati anthu osachimwa.

**70. “Kuyeretsa” ndiko kutani?**

Ndiye cuti Mulungu wasandutsa mitima ndi makhalidwe a ochimwa onse kukhala woyeria.

**71. “Kusandka ana a Mulungu” ndiko kutani?**

Ndiye cuti Mulungu watilandira kukhala m'mbumba yake ndi kukhala ana ake.

**72. Kodi Khristu adamvera ndi kuzunzidwa chifukwa cha yani?**

Osankhidwa ake, amene Atate ake adampatsa.

**73. Khristu adakhala moyo wotani pansi pano?**

Moyo wosauka ndi wozunzika.

**74. Khristu adafa imfa yotani?**

Imfa yowawa ndi yochitsa manyazi ya pamtanda.

*Vesi loloweza pamtima:*

Mbusa wabwino ndine. Ndipo nkhosa zanga ndimazidziwa, ndipo izozo Ineyo zimandidziwa, monga momwe Atate amadziwira Ine, nanenso nkuwadziwa Atatewo. Ndimatayirapo moyo wanga pa nkhosazo. (Yoh 10:14-15)

**PHUNZIRO 9**  
**ZA KULAPA NDI CHIKHULUPILIRO**

**75. Ndani adzapulumuke?**

Okhawo osankhidwa ake a Mulungu.

**76. Mudziwa bwanji kuti ndinu osankhidwa ake a Mulungu?**

Ndikalapa machimo, kukhulupilira Khristu, ndikukhala moyo oyera.

**77. Kulapa ndiko kutani?**

Kunena kuti ndachimwa, kudana ndi tchimo ndikulikana chifukwa Mulungu sakondwera nalo.

**78. Kodi kukhulupilira Khristu ndiko kutani?**

Kukhulupilira kuti Khristu yekha ndi amene angandipulumutse.

**79. Kupulumutsidwa ndiko kutani?**

Kukhala ndi ufulu ku mphamvu ya tchimo ndi kalandira moyo wosatha.

**80. Kalandira moyo wosatha ndiko kutani?**

Kudziwa ndi kusangalala ndi Mulungu mwa Khristu, lero mpaka nthawi zosatha.

**81. Mungalape ndi kukhulupilira Khristu mwa inu nokha?**

Ayi, sindingathe kuchita china chirichonse chabwino popanda mphamvu ya Mulungu Mzimu Woyera.

**82. Mungakhale nayo bwanji mphamvu ya Mulungu Mzimu Woyera?**

Ndiyenera kupemphera kuti Mulungu anditumizire Mzimu Woyera.

**83. Papita zaka zingati Ambuye Yesu atafa?**

Pafupifupi zaka 2000 zapitazo.

**84. Anthu oopa Mulungu adapulumutsidwa bwanji Khristu asanabwere?**

Pokhulupilira Mpulumutsi wodzabwerayo.

**85. Kodi adawonetsa bwanji chikhulupiliro chawo?**

Popereka nsembe zawo pa guwa la Mulungu.

**86. Nsembe zimenezi zimayimirira chiyani?**

Khristu, Kankhosa ka Mulungu amene anayenera kudzafera ochimwa.

*Vesi loloweza pamtima:*

“ Ndi kukoma mtima kwa Mulungu kumene kunakupulumutsani pakukhulupilira. simudapulumuke chifukwa cha zimene inuyo mudachita ayi, kupulumuka kwanu ndi mphatso ya Mulungu. Munthu sapulumuka chifukwa cha ntchito zake, kuwopa kuti angamanyade. (Aef 2:8-9)

**PHUNZIRO 10**  
**MAUDINDO ATATU A KHRISTU**

**87. Khristu ali ndi maudindo ati?**

Khristu ali ndi maudindo atatu.

**88. Maudindiwo ndiwo ati?**

Maudindowo ndi awa: Uneneri, Unsembe ndi Ufumu.

**89. Chifukwa chiyani Khristu ali Mneneri?**

Amatiphunzitsa za chifuniro cha Mulungu.

**90. Chifukwa chiyani Khristu ali Wansembe?**

Anafa chifukwa cha machimo athu ndipo amatinenera kwa Mulungu.

**91. Chifukwa chiyani Khristu ali Mfumu?**

Amatilamulira ndi kutiteteza.

**92. Chifukwa chiyani mukumusowa Kristu ngati Mneneri?**

Chifukwa ndine wosadziwa china chiri chonse.

**93. Chifukwa chiyani mukumusowa Khristu ngati Wansembe?**

Chifukwa ndine wochimwa.

**94. Chifukwa chiyani mukumusowa Khristu ngati Mfumu?**

Chifukwa ndine wofooka ndi opanda pake.

*Vesi loloweza pamtima:*

Pajatu Mulungu ndi mmodzi yekha, Mkhalapakati mmodzi yekhanso pakati pa Mulungu ndi anthu, munthu uja timati Khristu Yesu. (1 Tim 2:5)

**PHUNZIRO 11**  
**MALAMULO KHUMI**

**95. Kodi Mulungu adapereka malamulo angati pa phiri la Sinai?**  
Malamulo khumi.

**96. Kodi malamulo khumiwa amatchulidwano kuti chiyani?**  
Malamulo Khumi a Mulungu.

**97. Malamulo anayi oyamba amatiphunzitsa chiyani?**  
Kukonda Mulungu.

**98. Nanga malamulo asanu ndi limodzi otsiriza amatiphunzitsa chiyani?**  
Kukonda anzathu.

**99. Chidule cha malamulo onse khumi n'chotani?**  
Kukonda Mulungu ndi mtima wanga wonse, komanso kukonda anzanga monga ndidzikondera ine mwini.

**100. Mzangayo ndiye yani?**  
Mzangayo ndi aliyense amene ndiyenera kumuonetsa chikondi.

**101. Kodi Mulungu amakondwera ndi amene amkonda ndi kumvera malamulo ake?**  
Inde; Iye akunena kuti, “Akundikonda ndiwakonda, akundifuna adzandipeza.” (Miy 8:17)

**102. Kodi Mulungu sakondwera ndi onse amene samukonda ndi kumvera malamulo ake?**

Inde, “Mulungu amalanga anthu oyipa nthawi zonse.” (Mas 7:11)

*Vesi loloweza apamtima:*

*“Ndipo Yesu anati kwa Iye, Uzikonda Ambuye Mulungu wako ndi mtima wako wonse, ndi moyo wako wonse, ndi nzeru zako zonse. Ili ndilo lamulo lalikuru ndi loyamba. Ndipo lachiwiri lolingana nalo ndili: Uzikonda mnzako monga udzikonda iwe mwini” ( Mat 22:37-39)*

**PHUNZIRO 12**  
**LAMULO LOYAMBA MPAKA LACHITATU**

**103. Lamulo loyamba likuti chiyani?**

Usakhale ndi Milungu ina koma ine ndekha.

**104. Kodi lamulo loyamba litiphunzitsa chiyani?**

Kupembedza Mulungu yekha.

**105. Lamulo lachiwiri likuti chiyani?**

Usadzipangire fano kapena chirichonse chofanizira kanthu kena kalikonse kakumwamba kapena ka pa dziko lapansi, kafenango ka m'madzi a pa dziko. Usagwadire fano lirilonse kapena kumalipembedza, chifukwa ine \*Chauta, Mulungu, ndine Mulungu wosalola kupikisana nane ndipo ndimalanga ana chifukwa cha atate awo, kufikira mbadwo wachitatu ndi wachinayi. Komatu anthu ambirimbi a mibadwo yosawerengeka amene amandikonda, namatsata malamulo anga, ndimawakonda ndi chikondi chosasinthika.

**106. Kodi lamulo lachiwiri litiphunzitsa chiyani?**

Kupembedza Mulungu monga momwe Mulunguyo afunira.

**107. Lamulo lachitatu likuti chiyani?**

Usatchule pachabe dzina la Yehova Mulungu wako, chifukwa Mulunguyo sadzamleka aliyense wotchula pachabe dzina lakelo.

**108. Lamulo lachitatu litiphunzitsa chiyani?**

Kulemekeza dzina, mau ndi ntchito za Mulungu.

*Vesi loloweza pa mtima:*

Mau a Chauta ngangwiro, amapatsa munthu moyo watsopano. Umboni wa Chauta ngokhulupirika, umawapatsa nzeru amene alibe. (Mas 19:7)

## PHUNZIRO 13 LAMULO LA CHINAYI

### **109: Lamulo la chinayi likuti chiyani?**

Udzikumbukira tsiku la sabata, likhale lopatulika. Masiku asanu ndi limodzi uzigwira ntchito zako zako zonse. Koma tsiku la chisanu ndi chiwiri ndi la sabata loperekedwa kwa Yehova, Mulungu wako. Usamagwira ntchito pa tsiku limenelo iweyo, kapena ana ako, kapena antchito ako, kapena zoweta zako, kapena mlendo amene amakhala m'mudzi mwako. Paja pa masiku asanu ndi limodzi \*Chauta adalenga zonse za kumwamba ndi za pa dziko lapansi, nyanja ndi zonse za m'menemo, koma pa tsiku la chisanu ndi chiwiri adapumula. Nchifukwa chake adadalitsa tsiku la Sabata, nalisandutsa loyera.

### **110. Lamulo la chinayi litiphunzitsa chiyani?**

Kusunga tsiku la Sabata kuti likhale loyera.

### **111. Ndi tsiku liti pa mulungu lomwe ndi Sabata ya a Khristu?**

Tsiku loyamba la pa mulungu, lomwe limatchulidwa Tsiku la La Mulungu.

### **112. Chifukwa chiyani likutchulidwa Tsiku la Mulungu?**

Christu adauka kwa akufa pa tsiku limenelo.

### **113. Kodi pa tsiku la Sabata tichite chiyani?**

Kupemphera ndi kutamanda Mulungu, kumvetsera ndi kuwerenga mau a Mulungu, ndi kuchitira ena zabwino.

*Vesi loloweza :*

Nchifukwa chake tsono mpumulo wanga wa pa Sabata wawatsalirabe anthu a Mulungu.  
(Ahebri 4:9)

**PHUNZIRO 14**  
**LAMULO LA 5 MPAKA LA 7**

**114. Lamulo la chisanu likuti chiyani?**

Uzilemekeza atate ndi amayi ako, kuti masiku a moyo wako achuluke m'dziko limene Yehova Mulungu wako, adakupatsa.

**115. Lamulo lachisanu litiphunzitsa chiyani?**

Kukonda ndi kumvera makolo ndi aphunzitsi athu.

**116. Lamulo la chisanu ndi chimodzi likuti chiyani?**

Usaphe.

**117. Lamulo la chisanu ndi chiwiri litiphunzitsa chiyani?**

Kukhala mwamtendere ndi okondana m'maganizo, m'mawu ndi m'zochita zathu; ndi kupewa kusunga mkwiyo.

**118. Lamulo la chisanu ndi chiwiri likuti chiyani.**

Usachite chigololo.

**119. Lamulo la chisanu ndi chiwiri litiphunzitsa chiyani?**

Kukhala oyera mtima, malankhulidwe ndi makhalidwe athu.

**120. Lamulo la chisanu ndi chitatu likuti chiyani?**

Usaphe.

**121. Lamulo la chisanu n'chitatu litiphunzitsa chiyani?**

Kukhala wachilungamo ndi wogwira ntchito molimbika.

*Vesi loloweza pamtima:*

Inu ana, popeza ndinu ake a Khristu, muzimvera akukubalani mwa Ambuye, pakuti ichi nchabwino. (Aef 6:1)

**PHUNZIRO 15**  
**LAMULO LA 8 MPAKA LA 10**

**122. Lamulo la chisanu n'chinayi likuti chiyani?**

Usamunamizire mzako.

**123. Lamulo la chisanu n'chinayi litiphunzitsa chiyani?**

Kunena zonna; osati zonama.

**124. Lamulo la chikhumi likuti chiyani?**

Usasirire nyumba ya mzako, usasirire mkazi wa mzako kapena wantchito wake wa mwamuna kapena wamkazi, kapena ng'ombe yake, kapena bulu wake, kapena kalikonse ka mzako.

**125. Lamulo lachikhumi litiphunzitsa chiyani?**

Kukhala wokhutitsidwa mmoyo wathu.

**126. Alipo angatsate malamulowa bwino lomwe?**

Ai, palibe, kuyambira nthawi yomwe Adamu adachimwa palibe adasunga Malamulo Khumi bwino lomwe.

**127. Ntchito ya Malamulo Khumi kwa ife ndi yotani?**

Amatiphunzitsa udindo wathu ndi kutiwonetsa kuti tikusowa Mpulumutsi.

**128. Tingasunge bwanji Malamulo Khumi?**

Tiyenera kuwatsatira mwachikondi ndi mothokoza Ambuye Yesu.

*Vesi loloweza pa mtima:*

“Basi, zonse zamveka. Mfundu yeniyeni ya zonsezi ndi iyi: Uzimvera Mulungu, ndipo uzsata malamulo ake, pakuti umenewu ndiwo udindo wake onse wa munthu.” (Mlaliki 12:13)

**PHUNZIRO 16**  
**PEMPHERO LA AMBUYE**

**129. Kodi pemphero ndi chiyani?**

Pemphero ndiko kupempha kwa Mulungu zinthu zimene adalonjeza kuperekwa.

**130. Kodi tipemphere m'dzina la yani?**

M'dzina la Khristu yekha basi.

**131. Khristu adatipatsa chiyani chotiphunzitsa kupemphera?**

Pemphero la Ambuye.

**132. Nenani Pemphero la Ambuye.**

Atate athu a kumwamba, dzina lanu liyeretsedwe.

Ufumu wanu udze

Kufuna kwanu kuchitidwe

Monga kumwamba chomwecho pansi pano.

Mutipatse ife lero chakudya chathu chalero.

Mutikhululukire ife zochimwa zathu moga ifenso tiwakhulukira a mangawa athu.

Musatitengere ife kokatiyesa, koma mutipulumutse kwa oipayo.

Chifukwa wanu ndi ufumu, ndi mphamvu ndi ulemelero ndi ulemelero wanu nthawi zonse. Ameni.

**133. M'Pemphero la Ambuye, muli zopempha zingati?**

Zisanu ndi chimodzi.

*Vesi loloweza pamtima:*

“Pemphani ndipo chidzapatsidwa kwa inu, funani ndipo mudzapeza; gogodani, ndipo chidzatsegulidwa kwa inu” (Mat 7:7)

**PHUNZIRO 17.  
PEMPHO LOYAMBA MPAKA LACHITATU**

**134. Pempho loyamba ndi lotani?**

Dzina lanu liyeretsedwe.

**135. Mupempho loyamba timapempherera chiyani?**

Kuti ife ndi anthu ena onse alemekaze Dzina la Mulungu.

**136. Pempho lachiwiri ndi lotani?**

Ufumu wanu udze.

**137. Mupempho lachiwiri timapempherera chiyani?**

Mthenga Wabwino ulalikidwe padziko lonse lapansi, ndipo kuti ife ndi anthu ena onse tiukhulupilire ndi kuutsatira.

**138. Pempho lachitatu ndi lotani?**

Kufuna kwanu kuchitidwe, monga kumwamba chomwechonso pansi pano.

**139. Mupemphero lachitatu timapempherera chiyani?**

Kuti anthu onse padziko lapansi atumikire Mulungu monga momwe achitira angelo kumwamba.

*Vesi loloweza pamtima:*

Yehova, Ambuye wathu, Dzina lanu liposadi nanga pa dziko lonse lapansi! Inu amene munaika ulemelero wanu pa thambo la kumwamba” (Masalimo 8:1)

**PHUNZIRO 18**  
**PEMPHO LACHINAI MPAKA LACHISANU NDI CHIMODZI**

**140. Pempho lachinayi ndi lotani?**

Mutipatse ife chakudya chathu chalero.

**141. Mupempho la chinayi timapempherera chiyani?**

Kuti Mulungu atipatse zomwe tikuzisowa, za mzimu ndi zathupinso.

**142. Pempho lachisanu ndi lotani?**

Mutikhululukire ife machimo athu, monga ifenso tiwakhululukira amangawa athu.

**143. Mupempho lachisanu timapempherera chiyani?**

Kuti Mulungu atikhululukire zochimwa zathu chifukwa cha Khristu, ndi kutinso Mulungu awakhululukire amene anatichimwira.

**144. Pempho la chisanu ndi chimodzi ndi lotani?**

Musatitengere ife kokatiyesa, koma mutipulumutse ife kwa woipayo.

**145. Timapempherera chiyani mu pempho la chisanu ndi chimodzi?**

Kukti Mulungu atiteteze kumachimo.

*Vesi loloweza pamtima:*

Koma inu, yambani mwafunafuna Ufumu wa Mulungu ndi kumachita zimene lye akufuna, ndipo zina zonsezi zidzapatsidwa kwa inu. (Mat 6:33)

**PHUNZIRO 19**  
**NJIRA ZAKE ZA CHISOMO**

**146. Njira za chisomo ndi chiyani?**

Ndi njira zomwe Mulungu anazisankhiratu zotithandiza kuti tikule mwa Khistu.

**147. Njira zodziwika bwino zotithandiza kukula m'chisomo cha Mulungu ndizo ziti?**

Kuwerenga ndi kumva Mau a Mulungu, kulandira masakramenti ndi kupemphera.

**148. Masacrament alipo angati?**

Alipo awiri.

**149. Masakramentiwo ndiwo ati?**

Ubatizo ndi Mgonero wa Ambuye.

**150. Ndani anapanga masakramenti?**

Ambuye Yesu Khristu.

**151. Chifukwa chiyani Khristu anapanga masakramentiwa?**

Pofuna kusiyantsa ophunzira ake ndi anthu ena komanso kuwatonthoza mitima ndi kuwalimbikitsa.

*Vesi loloweza pa mtima:*

Yesu adadza pafupi nawauza kuti, "Mphamvu zonse zapatsidwa kwa Ine kumwamba ndi pa dziko la pansi. Nchifukwa chake mukani phunzitsani anthu a mitundu yonse ndi kuwabatiza iwo m'dzina la Atate, ndi la Mwana, ndi la Mzimu Woyer. Ndikuaphunzitsa, asunge zinthu zonse zimene ndinakulamulirani inu; ndipo onani, Ine ndiri pamodzi ndi inu masiku onse, kufikira chimariziro cha nthawi ya pansi pano (Mat 28: 18-20).

## PHUNZIRO 20 UBATIZO

**152. Ndi chizindikiro chiti chomwe chimagwiritsidwa ntchito pa Ubatizo?**

Kusamba ndi madzi.

**153. Chizindikiro chimenechi chitanthauzanji?**

Kutsukidwa ku machimo ndi mwazi wa Khristu.

**154. Kodi timabatizidwa m' dzina la ndani?**

M'dzina la Atate, ndi la Mwana, ndi la Mzimu Woyeria.

**155. Ndani oyenera kubatizidwa?**

Onse okhulupilira ndi ana awo.

**156. Chifukwa chiyani ana a anthu okhulupilira ayenera kulandira ubatizo?**

Chifukwa iwonso ndi ana a lonjezo la chipangano.

**157. Kodi Khristu amasamalira ana aang'ono?**

Inde; popeza akuti "Aloleni ana adze kwa ne, musawakanize; chifukwa ufumu wa Mulungu uli wao.

**158. Kodi ubatizo umakusandutsani kukhala yani?**

Kukhala wotsatira weniweni wa Khristu.

**159. Kodi ana wolandira ubatizo ndi akhristunso?**

Inde, koma okhawo amene alapa ndi mtima onse ndi kukhulupilira Khristu amapulumutsidwa.

*Vesi loloweza pa mtima:*

Paja zimene Mulungu adalonjeza zija, adalonjezera inuyo, ana anu ndiponso anthu onse okhala kutali, onse amene Ambuye Mulungu wathu adzawaitana. (Machitidwe 2:39)

**PHUNZIRO 21**  
**MGONERO WA AMBUYE**

**160. Mgonero wa Ambuye ndi chiyani?**

Kudya mkate ndi kumwa vinyo pofuna kukumbukira masautso ndi imfa ya Khristu.

**161. Mkatewo umaimirira chiyani?**

Thupi la Khristu lomwe linaonongedwa cifukwa cha machimo athu.

**162. Vinyo akuimirira chiyani?**

Mwazi wa Khristu okhetsedwa chifukwa cha chipulumutso chathu.

**163. Ndani ayenera kudya mgonero wa Ambuye?**

Okhawo amene alapa machimo awo ndi kukhulupilira Khristu kuti apulumuke komanso amakonda anzawo.

**164. Tilandire bwanji Mgonero wa Ambuye?**

Ndi chikhulupiliro komanso chikondi mmitima mwathu chifukwa cha Ambuye Yesu Khristu.

**165. Amene alandira Mgonero wa Ambuye moyenera  
amapindula chiyani?**

Amakula muuzimu ndi m'chisomo cha Mulungu.

**166. Amene salandira Mgonero wa Ambuye moyenera  
amalandira chiyani?**

Chiweruzo cha Mulungu.

*Vesi loloweza pa mtima:*

Pakuti nthawi zonse mukamadya mkate umenewu, ndi kumwa chikho chimenechi, mumalalika imfa ya Ambuye, kufikira akadze lye. (1 Akorinto 11:26)

**PHUNZIRO 22**  
**ZA CHIMALIZIRO**

**167. Kodi Kristu adakhalabe mmanda pambuyo pa imfa yake ya pamtanda?**

Ayi; adauka mmanda pa tsiku la chitatu la imfa yake.

**168. Kodi Khristu ali kuti?**

Kumwamba ndipo amatinenera kwa Mulungu.

**169. Kodi adzabweranso?**

Inde; patsiku lomaliza Khristu adzabweranso pa tsiku lomaliza kudzaweruza dziko la pansi.

**170. Chimachitika n'chiyani anthu akafa?**

Matupi awo amabwerera kufumbi, pomwe mizimu yawo imapita kudziko la mizimu.

**171. Kodi matupi a anthu akufa adzaukutsidwanso ndi moyo?**

Inde; lipenga likadzalira, akufa onse adzauka.

**172. Chidzachitika ndi chiyani kwa oipa onse pa tsiku lomaliza?**

Adzaponyedwa ku jehena.

**173. Jehena ndi chiyani?**

Ndi malo owopsya a mazunzo ndi chilango chosatha.

**174. Anthu abwino adzaona zotani?**

Adzatengedwa kupita kumwamba.

**175. Kumwamba ndiko kuti?**

Ndi malo a ulemelero ndi chisangalalo komwe anthu olungama adzakhalako ndi Ambuye nthawi zonse.

*Vesi loloweza pamtima:*

Taonani ndikukuuzani chinsinsi; sitidzagona tonse, koma tonse tidzasandulika, m'kamphindi, m'kutwanima kwa diso, pa lipenga lotsiriza; pakuti lipenga lidzalira, ndipo akufa adzakukitsidwa osabvunda, ndipo ife tidzasandulika. (1 Akorinto 15:52)

**PHUNZIRO 23.**  
**MBIRI YA CHIKONZEDWE CHA MPINGO I**

**1. Chikonzedwe cha Mpingo ndicho chiyani?**

Chikonzedwe cha mpingo kunali kusintha kwa maganizo kuchokera ku maphunzitso olakwika a Mpingo wa chi Roma ndi kuphunzitsa choona cha Baibulo.

**2. Kodi John Wyclife anali ndani?**

Ndi amene anatanthauzira Baibulo kupita ku chinenero cha chingerezi.

**3. John Huss anali yani?**

Anaphunzitsa zonna zazikulu za Baibulo ku dziko la kwavo ku Bohemia.

**4. Johann Gutenberg anali ndani?**

Anali mJeremani amene anapanga makina olembira oyambilira.

**5. Martin Luther anali ndani?**

Ndi amene anayambitsa Chikonzedwe cha Mpingo ku Germany pophunzitsa kuti anthu amapulumuka ndi chikhulupiliro chokha basi.

**6. Ulrich Zwingli anali yani?**

Ndi amene anayambitsa Chikonzedwe cha Mpingo ku Zurich, Switzerland.

*Vesi loloweza pamtima:*

Popeza kuti ponse pozungulira pali mboni zambirimbiro chotere, tiyeni tichotse kalikonse koticedwetsa, makamaka tchimo limene limatikangamira, ndipo tithamange ndi khama mpikisano umene tayambawu. ( Ahebri 12:1)

## **PHUNZIRO 24** **MBIRI YA CHIKONZEDWE CHA MPINGO II**

### **7. William Farel anali ndani?**

Analalikira mwa mphamu za Chikonzedwe cha Mpingo ku Geneva m'dziko la Switzerland.

### **8. John Calvin anali ndani?**

Anali mbusa wa chiFalansa amene anapangitsa maphunzitso ndi chipembedzo kukhala chabwino ndi cha mphamu mu nthawi ya Chikonzewe cha Mpingo.

### **9. John Knox anali ndani?**

Anali mbusa wa ku Scotland amene anaphunzitsa za Chikonzedwe cha Mpingo ku Scotlandeko komanso ndi amene anayambitsa chiPuresibeteriani.

### **10. Msonkhano wa ku Westminster ndi chiyani?**

Ndi msonkhano wa anthu a Mulungu amene anakomana ku Westminster Abbey ku London zaka 360 zapitazo pamene analemba buku la Kuulula Machimo komanso makatekisimu amene tikugwiritsa ntchito panowa.

*Vesi loloweza pamtima:*

Maso athu azipenyetsetsa Yesu ali woyambitsa chikhulupiliro chathu, ndiponso wochifikitsa pake penipeni; Chifukwa cha chimwemwe chimene chinkamudikira, Iyeyo adapirira zowawa zapamtanda. Adawanyoza manyazi a imfa yotere ndipo tsopano akukhala kudzanja la manja la mpando wachifumu wa Mulungu. (Aheberi 12:2)

## PHUNZIRO 25

### MFUNDO ZISANU ZA MAPHUNZITSO A CALVIN

#### **1. Mfundu zisanu za maphunzitso a Calvin ndi chiyani?**

Ndi mfundu zomwe zikupereka chidule cha maphunzitso a Baibulo a John Calvin okhudza chipulumutso.

#### **2. Mfundu yoyamba ya chipunzitso cha John Calvin ndi yotani?**

*Kuperewera kwathunthu:* Kutanthauza kuti munthu sangathe kupulumuka mwa iye yekha chifukwa mwachilengedwe chake ndiwochimwa pazochita zake, mmaganizo mwake ndi mzonena zake.

#### **3. Mfundu ya chiwiri ya chipunzitso cha Calvin ndi yotani?**

*\*Kusankhidwa kosayang'ana kuti tachita zakutizakuti:* kutanthauza kuti ake a Mulungu amasankhidwa ndi Mulungu mwini monga momwe lye kwamukomera osati chifukwa choti achita zabwino.

#### **4. Mfundu ya chitatu ya chipunzitso cha Calvin ndi yotani?**

*Kudzipereka kopanda malire:* kutanthauza kuti Khristu anazunzika ndi kutifera kuti apulumutse anthu ake osankhidwa.

#### **5. Mfundu ya chinayi ya chipunzitso cha Calvin ndi yotani?**

*Chisomo chosaletseka:* kutanthauza kuti osankhika ake a Mulungu adzapulumuka chifukwa cha Mzimu Woyeram amene adzautsa chikhulupiliro mwa iwo.

#### **6. Mfundu ya chisanu ya chipunzitso cha Calvin ndi yotani?**

*Kupilira kwa anthu oyera:* kutanthauza kuti mkhristu weniweni sadzaleka kukhala mkhristu.

*Vesi loloweza pamtima:*

Mauwa ali okhulupirika ndi oyenera konse kuti awalandire kuti Khristu Yesu anadza ku dziko lapansi kupulumutsa ochimwa; ndipo mwa iwovo ine ndiye wochimwa koposa. (1 Tim 1:15)